# KALATA YACHIWIRI YA YOHANE

1 Ndine mkulu wampingo, kulembera:

Mayi wosankhidwa ndi Mulungu ndi kwa ana ake amene ndimawakonda m'choonadi. Ndipo sindine ndekha amene ndimawakonda, komanso onse odziwa choonadi.
2 Timakukondani chifukwa cha choonadi
chimene chimakhala mwa ife ndipo chidzakhala mwa ife mpaka muyaya.

3 Chisomo, chifundo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate ndi kwa Yesu Khristu, Mwana wa Atate, zikhale ndi ife m'choonadi ndi m'chikondi.

## *Choonadi ndi Chikondi*

4 Ndinakondwera kwambiri nditapeza ana anu
ena akuyenda m'choonadi, monga Atate anatilamulira.
5 Ndipo tsopano, amayi wokondedwa,
sindikukulemberani lamulo latsopano koma lomwe lija takhala nalo kuyambira pachiyambi. Ine ndikukupemphani kuti tidzikondana wina ndi mnzake.
6 Ndipo chikondi ndiye kuyenda momvera
malamulo ake. Lamulo lake ndi lakuti mukhale moyo wachikondi monga munamva kuyambira pachiyambi.

7 Ndikunena zimenezi chifukwa anthu ambiri
onyenga, amene savomereza kuti Yesu Khristu anabwera monga munthu, akuyenda m'dziko

lapansi. Munthu aliyense otere ndi wonyenga
ndiponso wokana Khristu.
8 Chenjerani kuti mungataye chimene mwag-
wirira ntchito, koma chitani khama kuti muka-
landire mphotho yanu yonse.
9 Aliyense amene sasunga chiphunzitso cha
Khristu, alibe Mulungu. Koma amene amasunga
chiphunzitsochi, ameneyo alinso ndi Atate ndi
Mwana.
10 Ngati wina aliyense abwera kwa inu osa-
phunzitsa zimenezi, musamulandire m'nyumba
mwanu kapena kumupatsa moni.
11 Aliyense wolandira munthu wotere ndiye
kuti akuvomerezana nazo ntchito zake zoyipa.
12 Ndili nazo zambiri zoti ndikulembereni,
koma sindikufuna kuzilemba m'kalata. M'malo
mwake, ndikuyembekeza kufika kwanuko kuti
tidzakambirane nanu pamaso ndi pamaso,
potero chimwemwe chathu chidzakhala
chathunthu.
13 Ana a mlongo wanu wosankhidwa ndi Mu-
lungu akupereka moni.

# Biblica® Tsekulani Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero

## Chichewa: Biblica® Tsekulani Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero (Bible) of Malawi

copyright © 2016 Biblica, Inc.

Language: Chichewa

Contributor: Biblica, Inc.

Biblica® Open God's Word in Contemporary Chichewa™
Copyright © 2002, 2016 by Biblica, Inc.
"Biblica" is a trademark registered in the United States Patent and Trademark Office by Biblica, Inc. Used with permission.
Used with permission. All rights reserved worldwide.
All content on open.bible is made available under a Creative Commons Attribution-ShareAlike 4.0 License (http://creativecommons.org/licenses/by-sa/4.0/).
You are free to:
Share — copy and redistribute the material in any medium or format
Adapt — remix, transform, and build upon the material for any purpose, even commercially
Under the following conditions:
Attribution — You must attribute the work as follows: "Original work available for free at www.biblica.com and open.bible" Attribution statements in derivative works should not in any way suggest that we endorse you or your use of this work.
ShareAlike — If you remix, transform, or build upon the material, you must distribute your contributions under the same license as the original.
Use of trademarks: Biblica® is a trademark registered in the United States Patent and Trademark Office by Biblica, Inc. and may not be included on any derivative works. Unaltered content from open.bible must include the Biblica® trademark when distributed to others. If you alter the content in any way, you must remove the Biblica® trademark before distributing your work.
This translation is made available to you under the terms of the Creative Commons Attribution Share-Alike license 4.0.
You have permission to share and redistribute this Bible translation in any format and to make reasonable revisions and adaptations of this

translation, provided that:

- You include the above copyright and source information.
- If you make any changes to the text, you must indicate that you did so in a way that makes it clear that the original licensor is not necessarily endorsing your changes.
- If you redistribute this text, you must distribute your contributions under the same license as the original.

Pictures included with Scriptures and other documents on this site are licensed just for use with those Scriptures and documents. For other uses, please contact the respective copyright owners.

Note that in addition to the rules above, revising and adapting God's Word involves a great responsibility to be true to God's Word. See Revelation 22:18-19.

2021-11-15

---

PDF generated using Haiola and XeLaTeX on 18 Apr 2025 from source files dated 16 Nov 2021
f540eb34-4377-5601-9dcf-0a053d172faa